UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA LILONGWE M'DZINJA LA 2025-2026

DZINJA LA 2025/2026 MWACHIDULE

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/26.

Boma la Lilongwe likuyembekeza kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena yoposerapo mu nyengo ya dzinja la 2025/2026.

October 2025



Mvula yochuluka kufika mulingo wa 200-250mm ikuyembekezeredwa m'madera ambiri.
Madela ambiri atha kudzalandila mvula ya mulingo okhazikika kapena kuposera apo.

Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kudzagwa kuyambira sabata lachiwiri la mwezi wa December 2025.

November 2025



M'madera ambiri m'bomali adzalandira mvula ya mlingo okhazikika kapena kuchepera apo yokwana 20-50mm.

Koma m'madera a kwa Mazengera atha kudzalandira mvula yokwana mlingo wa 130-150mm

December 2025



Mvula yochuluka kufika mulingo wa 200-250mm ikuyembekezeredwa m'madera ambiri. Madera ena akwa SC Mtewa ndi SC Njewa atha kulandira Mvula yocheperako mulingo okhadzikika.
Madera ena onse atha kulandira mvula ya mulingo okhadzikika kapena kuposerapo
Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kuzagwa m'sabata yachiwiri ya December.

January 2026



Mvula yamlingo wokhazikika ndikuposerapo ikuyembekezeka m'madera ambiri mulingo okwana 250-300mm, koma mvula yocheperako ikuyembekezeka kugwa madera a ku mpoto kwa TA Chitukula ndi TA Chimutu mulingo osaposera 200mm.

Ng'amba yosapyola sabata imodzi ikuyembekezeka mu mweziwu.

February 2026



Madela ambiri a m'bomali akuyembekeza kulandira mvula yochepera mulingo wokhazikika mu mwezi umenewu, pomwe madela ambiri azalandire mvula yosaposera mulingo wa 200mm.

Ng'amba yosapyola sabata limodzi ikuyembekezeka m'mweziwu.

March 2026



Madera ambiri mu Lilongwe adzalandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera yokwanira pakati pa 150-200mm.

April 2026



Madera ambiri akuyembekereka kulandira mvula yosaposa mulingo wa 100mm.

Nyengo ya mvula ikuyembekezeka kufika kumapeto sabata lachiwiri la mwezi wa April 2026.

Boma la Lilongwe likuyembezera kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena yoposerapo.
Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kuzdagwa mu sabata yachiwiri ya December 2025, pamene mathero a mvula atha kukhala sabata yachiwiri mpaka sabata lachiwiri la April 2026. Pali chiopsezo cha ng'amba yosaposera sabata imodzi mu January ndi February 2026. Dzinja lonse likhala lotalika pakati pa masiku 120-130.

BUNDA			
MONTH	NORMAL RANGE		FORECAST
OCT	0.8	3.144	8.5
NOV	16.013	44.618	28.6
DEC	83.921	126.191	157.8
JAN	132.263	181.073	206
FEB	111.5	196.195	151.4
MAR	61.51	130.261	140.9
APR	5.498	22	47.4



Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2025

Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:

© Poster Template by Genigraphics® 1.800.790.4001 www.genigraphics.com